**ttb_Nya_0836_script**

**2 Atesalonika : 1:4-12**

**Mutu : Mazunzo, Kumwamba, ndi Gahena**

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni tiyambe ndi mau apa Ahebri 9:27, amene akuti, “Ndipo popeza kwaikikatu kwa anthu kufa kamodzi, ndipo atafa chiweruziro; kotero kristunsoataperekedwa nsembe kamodzikukasenza machimo a ambiri, adzaonekera pa nthawi yachiwiri, wopanda uchimo, kwa iwo amene amlindira, kufikira chipulumutso.”

Tsono mupologalamu yapita ija, tinali kukambirana kuchokera pa 2 Atesalonika 1:1-3, za mau oyamba. Ndipo lero pa 2 Atesalonika 1:4-12, tiona nkhani ya mazunzo, Kumwamba ndi Gahena.

Pano tiyeni tiyambe ndi mau akuti, ngakhale Mpingo sudzalowa mu nyengo ya ChizunzoChachikulu, koma udzadutsabe m’nyengo ya masautso.Tonse timakumana ndi mabvuto padziko lapansi pano.Tere ngati simukumana ndi mabvuto ndiye kuti zinthu zikuyendamolakwika m’moyo mwanu, chifukwa Mulungu amagwiritsa ntchito masautso kuti aphunzitse ana ake.

Tsono kupirira ndi mau ochititsa chidwi.Taonani amatanthauza kuti "kuyima pansi" kapena kuti "kusenza katundu wolemera."Anthu ambiri amafuna achokepo pansi pa chimene asenzacho.Munthu amene amapilira ndi munthu amene amanyamulabe katundu wolemerayo.Munthu wopirirayusataya kapena kutulakatundu chifukwa katunduyoakulemeraayi, popezaamazindikira kuti ali ndi udindo wonyamulakatunduyo.

4. Kotero kuti ife tokha tidzitamandira za inu m'mipingo ya Mulungu chifukwa cha chipiliro chanu ndi chikhulupiriro chanu, m'mazunzo anu onse ndi zisautsozo zimene mupirira nazo

Akhristu aku Atesalonika adali ndi umboni waukulu kumayiko amene anali pansi pa ulamuliro wankhanzawa Aroma. Aroma amawazunza kwambiri, kotero kuti akhristu aku Atesalonika adalipamasautso ndi mazunzo akulu.Koma ngakhale amakhala pa masautso akulu chikhulupiriro chawo chinali chosasunthika chifukwa anali ndi chipiriro.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tikunena kuti masautso padziko lapansi pano siachilendo.Mau a Mulungu amatiwuziratu kuti tidzakumana ndi masautso m’moyo uno.Iyi, ndiyo nkhani yomwe 1 Petro 4:12-16, adalembakuti, “Wokondedwa, musazizwe ndi mayesedwe amoto adakugwerani inu akhale chakukuyesani, ngati chinthu cha chilendochakuchitikirani inu: Koma popeza mulawana ndi Khristu zowawa zake, kondwerani: kutinsopabvumbulutso la ulemerero wake mukasangalalendikukondwerakwakukulukulu. Ngati munyozedwa pa dzina la Khristu, wodala inu; pakuti Mzimu wa ulemerero, ndi wa Mulungu apuma pa inu: kumbali yawo amuyankhulira Iye zoyipa, koma kumbali yanu Iye alemekezedwa. Koma asamve zowawa wina wa inu ngatiwambanda, kapena ngati mbala, kapena ngati wochita zoyipa, kapena ngati wodudukira nkhani za anthu ena. Koma ngati munthu wina akumva zowawa chifukwa choti ndi Mkhristu asachite manyazi; koma alemekeze Mulungu m’dzina ili.”

Anzanga musadabwe masautso akakugwerani.Ena amafunsa kuti sakudziwa kuti chifukwa chiyani Mulungu walora kuti

alowem'masautso ena ake.Nthawi zina zimawoneka ngati ndinu nokha amene muli m'masautsoamenewo.Ndifuna kukulimbikitsani kuti kuganiza kotere sikolondora. Masautso amene mukudutsamoangakule bwanji, alipo wina kwina kwake amenensoalim'masautso ofanana ndi omwewo. Sichachilendokwaokhulupirira kulowa m'mayesero kapena m'masautso. Pachifukwa ichi Petro akuchenjeza kuti tisamale kuti tisalowem'masautso chifukwa chakuti timachita zoyipa monga amachitira wakuba kapena wambanda.Ena amadzilowetsam'masautso chifukwa chopanda chilungamo.Ena amalowam'masautso chifukwa chothamangira nkhani zosawakhudza.Musadudukire nkhani za eni mungadzalowem'masautso.Masautso owayambadala ngati amenewa sangakupindulireni.Pali kusiyana kwakukulu pakati pa munthu amene amalowam'masautso chifukwa cha chipiriro chachikhulupiriro ndi anthu amene akulangidwa chifukwa akukhala mwa manyazi.Mulungu amagwiritsa ntchito masautso kuti ana ake akulem'chikhulupirirochachipiriro. Chikhulupiriro chachipirirochimatipatsa chiyembekezo cha kubwera kwa Ambuye.

5. Ndicho chitsimikizo cha chiweruziro cholungama cha Mulungu, kuti mukawerengedwe oyenera ufumu wa Mulungu umenensomudamva nawo zowawa.

Masautso athu sagwirizana kapena kuti sapereka chipulumutso chathu, koma amatipatsa chikonzero cha moyo osatha mtsogolo.Anzanga nkutheka kuti ena tikadzafikaKumwambatidzalakalaka kuti tikadasauka kuposa momwe timasaukira pansi pano ngakhale kuti pakadali pano timadandaula.

Anzanga, taonani kuti wokhulupirira amasautsidwa m'moyo uno pamene anthu osakhulupirirazimakhala ngati kuti zinthu zikuwayenderapamene sakukumana ndi masautso.Inu simuyenera kutaya mtima mukawona izi popeza ichi ndichitsimikizo cha chiweruzo cholungama cha Mulungu. Mulungu ndi wolungama ndipo amalora masautso kuti inu poyendamolungamamukawerengedwe oyenera mu ufumu wa Mulungu.

Paulo akuwalimbitsa mtima Atesalonika zakufunikakopilira pa masautso. Kupirira pa masautso kumapangitsam'khristukuwerengedwa oyenera muufumuwa

Mulungu. Kupilira pa zowawazo ndi kumene kumapereka chitsimikizo cha ufumu wa Mulungu. Monga sitikalowaKumwamba chifukwa cha ntchito zathu momwemonso sikungomva zowawa kumene kumatanthauza kuti munthu akalowaKumwamba ayi. Koma iwo amene amapiliraakamamva zowawa amakhala ndichitsimikizo cha ufumu wa Mulungu.

6. Powona kuti ndicho chilungamo kwa Mulungu kuti abwezerechinzunzo kwa iwo akukuchitirani inu chisautso.

Mulungu adzaweruza ndipo adzaweruzamolungama.Pa Aroma 9:14 Paulo adafunsa kuti;“Ndipo tsono tidzatani?Kodi chiripochosalungama ndi Mulungu?Msatero ayi.”Tamvani Yankho likunena kuti: “Musatero ayi!” kutsimikiza kuti chirichonse chimene Mulungu amachita chimakhala chabwino ndicholungama. Mulungu sangachitechina chirichonse cholakwa. Nthawi zina timadandaulatimawona ngati Mulungu sanachite bwino, ena amati amaganiza kuti Mulungu waafulatira. Uku,ndikudandaulamopanda chidziwitso chabe.Kumakhala kusadziwa njira za Mulungu.Mulungu amakhala ndi cholinga mu zinthu zonse zimene amachita. Mulungu ali ndi cholinga

cholungamapolora kuti mugwem'masautso, inde ngakhale m'Chizunzo Chachikulu. Safuna kuti muzunzike koma chimakhala chilango kwa anthu ochimwa.

7. Ndi kwa inu amene munzunzidwapumulani pamodzi ndi ife, ndipo pamene Ambuye Yesuadzabvumbuluka kuchokera Kumwamba pamodzi ndi angelo ake amphamvu.

Nkhani pano ikuti inu amene munzunzidwapumulani pamodzi ndi ife popeza Ambuye akubwera kudzaweruza. Akadzafikatidzapeza mpumulo kumasautso onse. Monga mipingoidapeza mpumulo kwa kanthawi Sitifanoataphedwa ndi miyala, ndichitsimikizo chakuti onse amene akuzunzidwaadzapeza mpumulo akadzabvumbuluka Yesu. Iyi, ndiyo nkhani ikukambidwa pa Machitidwe 9:31, pamene akuti, "Pamenepo mipingo ya m'Yudeya lonse ndi Galileya ndi Samariya idapumulanikhalayolimbikitsidwa ndi mtendere, nikhazikika; ndipo idayendam'kuwopakwa Ambuye ndi m'chitonthozo cha Mzimu Woyera, nichuluka." Kutanthauza kuti pobvumbuluka Yesu okhulupirira onseadzapumula kumasautso onse ndi ntchito zonse zolemetsa zadziko lapansi.Panthawiyiokhulupiriraadzapumula pamodzi ndi atumwi komanso okhulupirira ena.

Yesu adzabvumbuluka kuchokera Kumwamba pamodzi ndi angelo ake amphamvu. Palibe amene adamuwona Yesu ndi maso kuchokera pamene Yesu adakweraKumwambandikubisidwa ndi mitambo.Sitifano ndi Paulo okhaadamuona ndi maso achikhulupiriro. Koma patsiku limene adzabvumbulukandipo aliyense adzamuwona akubwera ndi angelo kuchokera Kumwamba. Adzabvumbuluka pamodzi ndi angelo ake amphamvu mu ulemelero wake. Adzafika ndi angelo ake amene amamutumikirandikumulambira ndipo angelowo ndi amphamvu koposa zinthu zina zirizonsezolengedwa. Mphamvu za angelo a Mulungu timawerenga pa 2 Mafumu 19:35 pamene kuti, “m’ngelo m’modzi anakantha anthu ambiri okwanira 185, 000 kupheratuonsewo.”Kutsindika kunena kuti Yesu sadzabvumbuluka ndi m’ngelo m’modzi ayi chifukwa akutiwuza kuti ‘Yesu adzabvumbuluka kuchokera Kumwamba pamodzi ndi angelo ake amphamvu.

8. M'lawilamoto, ndi kubwezera chilango kwa iwo osadziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu.
9. Amene adzalangidwa ndicho chiwonongekochosathachochokera ku nkhope ya Ambuye ndi ku ulemerero wa mphamvu yake.

Mau a Mulungu safotokoza zambiri za Kumwamba kapena zakuJahena. Ndikukhulupirira kuti Mulungu adachita izi kuti tingasokonezeke chifukwa anthu akadayambakumangoganiza za moyo wakumwambaosakhalam'moyo wa phindu padziko lapansi pano.  Mulungu akufuna tikakhale naye Kumwamba komanso ali nafe cholinga pansi pano.  Choncho tiyenera kukhala ndicholinga chofuna kukwaniritsa cholinga cha Mulungu pansi pano tisanapite Kumwamba.

Mau a Mulungu safotokozanso zambiri zakhalidwe la moyo wa anthu ochimwa.  Komabe chithunzi chimene chimawonekam'Mau a Mulungu chimene adabvumbulutsa Mzimu Woyera ndichomvetsa chisoni ndichowopsa kwambiri.Pankhani ya chiweruzo, palibe

pamene timawerengazosonyeza kuti Mulungu adzaweruzamwachipongwe kapena mofunakubwezera choyipa ayi.Mulungu adzaweruza monga mwa chiyero ndi chilungamo chake.Mau a Mulungu amakambazokwanirakutichenjeza za chilango cha ku Jahena.Ngakhale kuti Mau a Mulungu sanachite kukamba nkhani yonse yokhudza Gahena sizitanthauza kuti Jahenakulibeayi.Ndipo dziwani kuti zambiri zimene Mau a Mulungu amanena za Gahena adanena ndi Ambuye Yesu kuposa wina aliyense.Gahena ndi malo owopsa kwambiri.Tamvani mau a Paulo pa 2 Atesalonika 1:8-9, akuti,“M’lawilamoto, ndi kubwezera chilango kwa iwo osadziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Amene adzalangidwa ndicho chiwonongekochosathachochokera ku nkhope ya Ambuye ndi ku ulemerero wa mphamvu yake.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani ikuti anthu ambiri amanyozera nkhani yaku Gahena koma ngakhale akayikirendikunyozerasizitanthauza kuti Gahena kulibe ayi.Tikunena kuti inumusadzipusitse ndi maganizo anu.Dziwani kuti Gahena ilipo ndithu ndipo Yesu akubwera posachedwa.Akadzafikachoyambaadzatengaokhulupirira kuchoka

padziko lapansi ndipo kubwera kwake kotsatirakudzakhalakochititsa mantha kwa onse ochimwa. Kunena kuti kubweranso Yesu kudzakhala chiweruzo kwa onse osadziwandikukana Mulungu, kwa onse amene adakanakukhulupirira Uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Koma kudzakhala moyo wosathakwa onse amene adadziwa Yesu Khristu, amene adatumidwa pansi pano kuchokera Kumwamba. Mau a Mulungu akunena za moyo wosatha motere: “Ndipo moyo wosatha ndi uwu, kuti akadziwe Inu Mulungu wowona yekha, ndi Yesu Khristu, amene Inu mudamtuma” (Yohane 17:3). Kodi inu mukuganiza kuti mukalowa ku moyo wosatha chifukwa mumachita ntchito zabwino?Koma taonani mau a Mulungu akuyankha za ntchito yabwino pa Yohane 6:29, pamene akuti: “Ntchito ya Mulungu ndi iyi, kuti mukhulupirire Iye amene Iyeyoadamtuma.”

Ndiye tikunenetsa kuti nkhani ya Gahena ndi chiweruzo, anthu ambiri sitifunakuyimva.Mukamvetseramaumboni, mudzamva anthu akunena kuti ine ntchito yanga ikuyenda bwino kapena

malonda anga akuyenda bwino.Ena akuti ine banja langa likuyenda bwino.Sitikumva zambiri zimene adatichitira Ambuye Yesu.Ndiwochepa amene amanena mwachimvekere kuti ine ndinali wochimwa ndipo ndinatayikamwakutindimayenera kupita kuchilangochaku Gahena.Koma Ambuye Yesu adandipulumutsa.Chofunika kwambiri ndikutsindika kuti Yesu Khristuadakupulumutsani ku chiyani.Chifukwa chimene Yesu Khristuadabwerera padziko lapansi ndikutiadzakulanditseni ku moyo wachitayiko ndi chilango chosatha ku Gahena. Yesu adadzakudzapulumutsachotayikacho! Adadzakudzalanditsainu ndi ine kuchilango cha ku Gahena.Kodi inu mulinawo umboni umenewu?

Pachifukwa ichi ndi anthu ochepa masiku ano amene amalimba mtima kuwuza anthu ndi kulalikira zakuti munthu osakhulupirirandiwotayika.Anzanga, taganizanimukadakhala kuti munali m'nyumba imene imayaka inu muli mtulo.Munthu wina ndikuthamangira ku nyumbakondikulowa moto uli lawilawindikukupulumutsani ku moto wowopsawo.Kenako munthu

uja ndikupita nanu kunyumba kwake kuti mukhale mwana wake nakupatsani zinthu zambiri zapamwamba. Kodi tsiku lina simungamuthokonze pa gulu la anthu, chifukwa chakuti adakupangani kuti mukhale mwana wake? Ine, ndikukhulupirira kuti nkoyenerakutero. Kutsindika kunena kuti ndikofunika kwambiri kumuthokoza kuti munthu ameneyu sanasamalezamoyowake pamene adalowa m'nyumba moto wolusaukuyakandikukupulumutsani ku imfa. Palibe chinthu chabwino chimene mukadakhala nacho mukadapsyera m'nyumba muja munthu uja akadapandakuyika moyo wake pachiswe kuti akupulumutseni.

Tsono nkhani yonseyi ikulinga pakuti chiweruzo cha anthu otayikachikubwera ndithu.Tere, inu mukakhalabeotayikaosakhulupirira, mudzaweruzidwa.Tikunena kuti lero lino ngati mumva Uthenga Wabwino, musazengereze ayi, koma muyenera kupereka moyo wanu kwa Ambuye Yesu kuti akhale Mbuye ndi Mpulumutsi wanu.

10. Pamene adzadzakudzalemekezedwa mwa oyera mtima ake ndi kukhala woyamikiridwa ndi onse wokhulupirira (pakuti mudakhulupirira umboni wathu tidauchitakwa inu) m'tsiku lija.

Paulo pano akunena kuti pobwera Ambuye Yesu padziko lapansi patsiku lachiweruzookhulupirira kapena kuti oyera mtima onseadzamulemekeza Kristu.Kunena kuti tsiku limenelo Yesu amene ananyozedwa ndi anthu osakhulupiriraadzalemekezeka. Tsiku limenelo Yesu adzalemekezedwa ndi anthu oyera mtima chifukwa adzawonaulemelero wake ndi kuwona ukulu ndi mphamvu yake. Tsiku limeneo oyera mtima adzawona chigonjetso cha Ambuye Yesu ndipo Yesu Khristu adzalemekezedwa mwa onse oyera mtima.

Tsiku lobwera Ambuye chisomo chake ndi mphamvu yake idzawonekera kudzera mwa anthu amene adawapulumutsa.Mphamvu yake idzawonekera pomwe osakhulupirira onse adzalangidwa.

11. Chomwechonso tikupemphereraninso nthawi zonse, kuti Mulungu wathu akakuyeseni inu oyenera kumayitanidwe awa, ndikukwaniritsa chokoma chonse cha ubwino wake ndi ntchito yachikhulupiriro ndi mphamvu;

12. Kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Khristulilemekezedwe mwa inu, ndi inu mwa Iye, monga mwa chisomo cha Mulungu wathu ndi Ambuye Yesu Khristu.

Pano Paulo akuwuza Atesalonika kuti amawapempherera nthawi zonse.Ngakhale sanali pakati pawo komabeamawakumbukira.Ichi, ndi chinthu chopambana kwambiri chimene inu mungachitireena..Kupemphelera ena kumasonyeza kuti umawafunira zabwino anzako.Tawonaniuwu, ndiwo unali moyo wa Paulo kupempherera Atesalonika. Kodi inu mulinawo mtima uwu?

Tamvani Paulo akunena kuti dzina la Ambuye wathu Yesu Khristulilemekezedwe mwa inu.Tidayitanidwa ndi Mulungu kuti tiyende moyo wachiyero. Tidayitanidwa kuti tichoke ku m’dima ndikuyenda ndi Ambuye mu ufumu ndi ulemelero wake.Tikuyenerakuyendamolemekeza dzina la Yesu Khristu

Ambuye wathu. Tiyenera kupemphera kuti tikayendemolemekeza Ambuye Yesu chifukwa mwa ife tokha tilibe chimene chingatiyenerezekuyendamolemekeza dzina la Ambuye. Tisowa kuti Ambuye mwini wake amene adatiyitanaatipatse mphamvu yotitikayendemolemekezadzina lake.

Ndikukwaniritsa chokoma chonse cha ubwino wake ndi ntchito yachikhulupiriro ndi mphamvu: Chokoma chonse cha ubwino wake ndi ntchito yachikhulupiriro zimachokera ku chisomo cha Mulungu. Kutanthauza kuti Paulo amapemphera kuti ntchito ya chisomo cha Mulungu ikapitilirekuwonekera mu ntchito zawo zonse.Ntchito yachikhulupiriroimagwirika mu mphamvu ya chisomo cha Mulungu. Ntchito imene ingalemekeze ndi kuwonetsa mphamvu ya chisomo cha Mulungu imachokerakwa Mulungu amene amayigwira kufikira kuyimaliza mwa onse amene amakhulupirira Mulungu.

Wokondedwa tiyeni titsirize ndi mau akuti, tikayendamoyeneramayitanidwe athu, dzina la Ambuye wathu Yesu Khristulimalemekezedwa.Ili, likhale khumbolathu kuti dzina la

Ambuye wathu Yesu Khristulizilemekezedwam’mayendedwe athu.Zofuna zathu zina zonse zikhale zotsatira khumbo limeneli. Ntchito zathu zabwino ziziwonekera pakati pa anthu kuti anthu ena azilemekeza Mulungu ndikuti Yesu Khristuazilemekezedwa ndi moyo wathu komanso mwa ife.Kodi inu,mukuyendamolongosoka kuti dzina la Ambuye Yesu Khristulikulemekezedwa?Kunena kuti muli ndi umboni kuti Ambuye akulemekezeka mwa inu?

Lero tilekeza pano.Ndipo timasanthula 2 Atesalonika 1:4-12, tiona nkhani ya mazunzo, Kumwamba ndi Gahena.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!